Mmene Kutumizirana Zithunzi Kungakhudzire Mbiri Yanu

Werengani zochitika zotsatirazi ndi kuyankha mafunso kuti muone mmene zithunzi zanu zingakhudzire mbiri yanu.

CHOCHITIKA #1

Yerekezerani kuti ndinu woyang'anira kampani inayake yomwe ndi yodziwika bwino ndipo mukufuna kulemba ntchito achinyamata. Chifukwa choti achinyamatawo azidzachita zinthu m'malo mwa kampani yanu, mukuyembekezera kuti iwo azidzachita zinthu m'njira imene sidzaipitsa mbiri ya kampani yanuyo.

Ndiyeno mnzanu amene mumagwirizana naye kwambiri wabwera kudzafunsira ntchitoyo. Pansipa, lembani dzina la mnzanu weniweni amene mukuganiza kuti mukhoza kumulemba ntchitoyo.



Dzina: _____

Kenako pitani pamalo a mnzanuyo a pa intaneti omwe amatumizira ena zithunzi. Onani zithunzi zake, ndemanga zake, ndipo kenako yankhani mafunso otsatirawa:



Kodi munthu ameneyu adzachititsa kuti mbiri ya kampani yathu ikhale yabwino kapena yoipa?

_____

_____

Potengera zimene ndaonazi, kodi munthu ameneyu ndingamulembe ntchito?

_____

_____

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

CHOCHITIKA #2

Yerekezerani kuti mukupita kukafunsidwa mafunso kuti akulembeni ntchito. Munthu amene mukuyembekezera kuti adzakhala bwana wanu ali ndi bizinesi imene ikuyenda bwino kwambiri. Iye akufuna atalemba ntchito achinyamata. Chifukwa choti anthu amene awalembe ntchitowo azidzachita zinthu m'malo mwa kampaniyo, iye akuyembekezera kuti anthuwo azidzasonyeza makhalidwe abwino.



Ngati muli ndi malo otumizira zithunzi a pa intaneti, pitani pamalo anuwo ndipo yang'anani mwachidwi zimene zilipo. Kenako lembani zinthu zomwe mukuganiza kuti munthu amene mukuyembekeza kukulembani ntchito angaganize zokhudza inuyo poganizira zithunzi zanuzo komanso ndemanga zomwe munalembapo.

_____

_____

_____

_____

Zithunzi zingapangitse anthu kuganiza zinthu zosiyanasiyana zokhudza mbiri ya wotumizayo. Mwachitsanzo, anthu akhoza kukhala ndi maganizo awiri osiyana okhudza munthu amene chithunzi chake chili pamwambapa.

A. Ena angaganize kuti ndi wolimba mtima

B. Ena angaganize kuti ndi wosasamala

Malinga ndi zithunzi zimene zili m'munsimu, lembani zinthu ziwiri zofotokoza mbiri ya munthuyo.

A. _____

B. _____

A. _____

B. _____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania